# NDONDOMEKO YA MULUNGU YA CHIPULUMUTSO YOSAVUTA

## NDEMANGA:

1 Yohane 5 vs 13 izi ndakulemberani kuti mudziwe kuti muli ndi moyo wosatha, inu amene mukhulupilira dzina la Mwana wa Mulungu.

## 1. TONSE NDIFE OCIMWA

1 Yohane 1 vs 8 Tikati kuti tiribe ucimo, tidzinyenga tokha, ndipo ma ife mulibe coonadi.

1 Yohane 5 vs 16 – 17 wina akaona m'bale wace alikucimwa cimo losati la ku imfa, apemphere Mulungu, ndipo iye adzampatsira moyo wa iwo akucita macimo osati aku imfa.  Pali cimo la ku imfa, za ililo sindinena kuti mupemphere.  cosalungama ciriconse ciri ucimo, ndipo pali cimo losati la ku imfa.

1 Yohane 3 vs 6 Yense wakukhala mwa iye sacimwa, yense wakucimwa sanamuona iye, ndipo sanamudziwa iye.




**TONSE TINACIMWA**

## 2. PALI DIPO LA UCIMO

1 Yohane 5 vs 19 Tidziwa kuti tiri ife ocokera mwa Mulungu, ndipo dziko lonse lapansi ligona mwa woipayo.

1 Yohane 5 vs 12 Iye wakukhala naye mwana ali nao moyo, wosakhala ndi mwana wa Mulungu alibe moyo.

1 Yohane 3 vs 15 Yense wakudana ndi m'bale wace ali wakupha munthu, ndipo mudziwa kuti wakupha munthu aliyense alibe moyo wosatha wakukhala mwa iye.

# 3. YESU ANAFA NDIPO ANALIPIRA MACIMO ATHU PA MTANDA

1 Yohane 4 vs 10 Umo muli cikondi, sikuti ife tinakonda Mulungu, koma kuti iye anatikonda ife, ndipo anatuma Mwana wace akhale ciombolo cifukwa ca macimo athu.



**KRISTU ANAFERA OCIMWA**

1 Yohane 4 vs 2 – 3 M'menemo muzindikira Mzimu wa Mulungu, Mzimu uli onse umene ubvomereza kuti Yesu Khristu anadza m'thupi, ucokera mwa Mulungu.  Ndipo Mzimu uli wonse umene subvomereza Yesu sucokera kwa Mulungu, ndipo uwu ndiwo Mzimu wa wokana umene mudamva kuti ukudza, ndipo ulimo m'dziko lapansi lomwe.

1 Yohane 5 vs 11 ndipo uwu ndi umboniwo, kuti Mulungu anatipatsa ife moyo wosatha, ndipo moyo umene uli mwa Mwana wace.

# 4. TIIKE CIKHULUPIRO NDI CIYEMBEKEZO CATHU MWA YESU YEKHA

1 Yohane 5 vs 14 – 15 Ndipo uku ndi kulimbika mtima kumene tiri nako kwa iye, kuti ngati tipempha kanthu monga mwa cifuniro cace, atimvera.

AROMA 10 vs 9, 10, 13 kuti ngati uzabvomereza m'kamwa mwako Yesu ndi Ambuye ndi kukhulupira mu mtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka. Pakuti ndi mtima munthu akhulupilira kutengapo cilungamo, ndi kamwa abvomereza kutengapo cipulumutso. – pakuti amene aliyense adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka.

*Ngati ukufuna kulandira Yesu Kristu monga mpulumutsi ndi kulandira cikhululukiro cocokera kwa Mulungu, pempherani motere, komatu kulankhula pemphero limeneri olo lina lirilonse sikungakupumutseni. Ndikukhulupilira mwa Yesu Kristu kokha kumene kungakupatseni kukhulukidwa kwa macimo. Pemphero limeneri ndi njira yoonetsa kwa Mulungu cikhulupiliro canu mwa iye cifukwa cokukhulululukirani.*



*AMBUYE*

*NDIKUDZIWA NDINE OCIMWA, NDIKUDZIWA NDINE OYENERA KULANDIRA CILANGO CA MACIMO ANGA. KOMANO, NDIKUKHULUPILIRA INU YESU KRISTU MONGA MPULUMUTSI WANGA. NDIKUKHULUPILIRA IMFA NDI KUUKA KWACE KWANDIPEZETSA CIKHULUKIRO. NDIKUKHULUPILIRA YESU NDIPO INU YESU YEKHA NGATI MPULUMUTSI NDI MBUYE WANGA. ZIKOMO AMBUYE PONDIPULUMUTSA NDI KUNDIKHULUKIRA INE. AMEN*